

-Ngati m'mene a Isirayele analili olephera kuzipulumutsa okha kwa Farawo, anthu onse nawonso ali olephera kudzipulumutsa okha kwa Satana.

-Ngati m'mene analili Mose polephera kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo, palibenso munthu wina aliyense amene angathe kutipulumutsa ife kwa Satana.

-Ngati m'mene analili Mulungu yekha kuti ndi amene anali osalephera kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo, Mulungu yekha ndi amene angathenso kuŵapulumutsa anthu onse kwa Satana.

PHUNZIRO LA 26

1. Kodi amene anapereka maloto kwa Farawo anali ndani?

-Mulungu.

2. Kodi maloto oyamba amene Mulungu anaŵapereka kwa Farawo anali otani?

-Ng'ombe zisano ndi ziiri zowonda zinadya ng'ombe zisano ndi ziiri zonenepa.

3. Kodi maloto achiŵiri amene Mulungu anapereka kwa Yosefe anali otani?

-Masache asano ndi awiri owonda a tirigu anadya masache asano ndi awiri onenepa a tirigu.

4. Kodi amene anapupatsa Yosefe matanthawozo a maloto a Farawo anali ndani?

-Mulungu.

5. Kodi maloto awiriwa ankamasulira chiyani?

-Zaka zisano ndi ziiri za zokolola zambiri zidzadyedwa ndi zaka zisano ndi ziiri za njala.

6-Kodi Mulungu amatha kuŵatsogolera zochita anthu amene sakumukhulupiliranso lye?

-Inde.

7. Kodi Mulungu anaŵakwanilitsa bwanji maloto amene anamupatsa Yosefe ali mwana aja?

-Mulungu anamusankha Yosefe kukhala nduna yayikulu kwambiri ya dziko lonse la Ejipito.

8. Kodi chifukwa chiyani Yakobo anatenga banja lake lonse ndikupita nalo ku Ejipito?

-Chifukwa chakuti Yosefe ankakhala ku Ejipitiko.

-Chifukwa chakuti kunali chakudya chambiri ku Ejipitiko.
-Chifukwa chakuti Farawo nayenso anamupempha Yoko-bo kuti adzikakhala ku Ejipito.

-Pamene Yokobo ndi ana ake amuna pamodzi ndi maban-ja awo ankapita ku Ejipito, anali okwana makumi asano ndi aŵiri.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:1-5

1-Nawâ ana a Yokobo amene anapita ku Ejipito pamodzi ndi Yokoboyo ndi mabanja awo omwe:

2-Rubeni, Simiyoni, Levi, Yuda,

3-Isakara, Zebuloni, Benjamini,

4-Dani, Nafutali, Gadi, ndi Asere.

5-Chiŵerengero chenicheni cha anthu obadwa mwa Yokobo chinali makumi asano ndi aŵiri. Yosefe anali atakhazikika kale ku Ejipito.

-Kodi dzina latsopano limene Mulungu anaperekwa kwa Yakobo linali ndani?

-Isirayele.

-Zidzukulu za Aburahamu, Isaki ndi Yokobo nazonso zinkatchedwa Isirayele kapena a Isirayele.

-Yokobo ndi ana ake amuna pamodzi ndi mabanja awo, anakhala ndi Yosefe ku Ejipito kwa zaka zambiri.

-Njala itatha, Yosefe pamodzi ndi abale ake anapitilizabe kukhala ku Ejipito.

-Bambo awo, Yokobo, anamwalira koma Yosefe ndi abale ake anapitilizabe kukhala ku Ejipito.

-Kenako, Yosefe pamodzi ndi abale ake aja anamwaliran-

wo?
Iyayi.

-Mose anayesa kuti aŵapulumutse a Isirayele kwa Farawo, ndipo anamupha mu Ejipito m'modzi.

-Koma Farawo anadziŵa kuti Mose wapha mu Ejipito.

-Kodi Farawo anachita chiyani?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:15

15-Tsopano Farawo atamva, anayetsetsa kuti aphe Mose, koma Mose anathâŵa nakakhala ku dziko la Midyani.

-Farawo anadziŵa kuti Mose wapha mu Ejipito.

-Chomcho Farawo anayesa kuti amuphe Mose.

-Mose anagwidwa ndi mantha ndipo anathâŵa.

-Mose anathâŵira ku dziko la Midyani.

-Kodi Mose anakatha kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo?

Iyayi.

-Mose anayesa kuti aŵapulumutse a Isirayele kwa farawo koma analephera.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuŵapulumutsa a Isirayele kwa Farawo?

Mulungu.

-Ngati m'mene a Isirayele analili omagwidwa ndi Farawo, anthu onse nawonso ali omangidwa ndi Satana.

-Kodi Satana angayiletse tchito ya Mulungu?

-Iyayi.

-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.

-Mulungu anaŵatchinjiliza a Isirayele, ndipo adzŵatchinjilizanso anthu onse okhulupilira mwa lye.

-Mose anakulira mnyumba mwa Farawo, mpaka anafika pa ukulu.

-Tsiku lina, Mose anapita kukawona m'mane a Isirayele ankavutikira pansi pa ukapolo uja.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:11-14

11-Tsiku lina, Mose atakula ndithu, anapita kukacheza kwa anthu a mtundu wake uja, ndipo adawona m'mene amkaŵagwiritsira ntchito mowazunza kwambiri. Adawona Muejipito wina akumenya Muheberi, m'modzi mwa anthu a mtundu wake.

12-Chomcho Mose atayang'ana uku ndi uku, nqwona kuti kulibe anthu, anamupha Muejipitoyo nakwilira mtembo wake mu mchenga.

13-M'mawa mwake atabweranso, adawona kuti a Heberi aŵiri akumenyana. Mose anamufunsa olakwayo kuti, Chifukwa chiyani ukumumenya mzako?"

14-Iye uja anamufunsa Mose kuti, "Kodi ndani amene anakuyika kuti udzitilamlira ndi kumatiŵeruza? Kodi ukufuna kuti undiphe ngati m'mene unamuphera Muejipito uja?" Pameneopo Mose anachita mantha kwambiri ndipo anaganiza mu mtima mwake kuti, "Ha, anthu akuzidziŵa zimene ndidachita zija!"

-Kodi a Isirayele anakatha kudzipulumutsa okha kwa Fara-

so koma a Isirayele anapitilizabe kukhala ku Ejipito.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:6

6-Tsopano Yosefe anamwalira, abale ake ndi m'bado wawo wonse uja adamwaliranso.

-Chifukwa chakuti a Isirayele sanabwererenso kwawo ku dziko la Kanani, ndipo anapitilirabe kukhala ku Ejipito, anasanduka kukhala anthu ambiri.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:7

7-Koma zidzukulu za Isirayele zinabereka ana ambi- rimbiri. Anachulukana nakhala amphamvu kwambiri ndipo anadzadza m'dzikolo.

-Patapita zaka zambiri, mfumu ya ku Ejipito, Farawo, anamwalira.

-Kenako, analowâ Farawo watsopano.

-Farawo watsopanoyo sanali wabwino ngati Farawo oyamba uja.

-Farawo watsopanoyo anali woyipa kwambiri.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:8-11

8-Pambuyo pake panaloŵa mfumu ina imene siyinadziŵe za Yosefe.

9-Mfumuyo inaŵawuza anthu ake kuti, "A Isirayelewa akuchulukana kwambiri, ndipo ndi amphamvu kwambiri kupambana ife.

10-Mvetsani tsopano, ife tichite nawo mwanzeru anthu ameneŵa. Tiŵachenjerere kuti asachuluke, iwo an- gathe kudzaphatikizana ndi adani athu, nadzalimbana ndi ife, kenako kudzachoka m'dziko mwathu muno.

11-Tsopano anayika akapitawo awo oŵagwiritsa mwamkhaza ntchiti yolimba a Isirayelewo, kuti pakutero aŵafowoketse. A Isirayelewo anamumangira Farawo mizinda ya Pitomu ndi Ramsesi, kumene a Ejipito ankasunga chakudya chawo.

-Kodi Farawo watsopanoyo anachita chiyani kwa a Isirayele?

-Anaŵasandutsa a Isirayele onse kukhala akapolo.

-Kodi chifukwa chiyani Farawo anaŵasandutsa a Isirayele onse kukhala akapolo?

-Farawo ankawopa kuti a Isirayele angadzalande dziko lake.

-Kodi chifukwa chiyani Farawo ankawopa kuti a Isirayele angadzalande dziko lake?

-Chifukwa chakuti a Isirayele anachulukana kwambiri.

-Kodi amene ankamutsogolera Farawo kuti aŵasandutse a Isirayele onse kukhala a kapolo anali ndani?

-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Satana ankafuna kuŵawononga a Isirayele?

-Chifukwa chakuti Satana ankadziŵa kuti Mulungu analonjeza zutumiza Mpulumutsi kuditira mwa a Isirayele.

-Satana amadana ndi Mulungu.

-Satana amadana ndi anthu onse.

-Satana sankafuna kuti Mulungu atumize Mpulumutsi kuditira mwa a Isirayele.

-Satana sankafuna kuti Mpulumutsi adzabwere kudzaŵapulumutsa anthu.

-Mulungu anatumiza mwana wa mkazi wa Farawo oyipa uja kukamulera Mose.

-Ndipo Mose ankakhala ndi Farawo oyipa uja ndi mwana wake wa mkaziyo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutumiza mwana wa mkazi wa Farawo kuti amulele Mose?

-Chifukwa chakuti Mulungu anakonza zoŵatsogolera a Isirayele kuditira mwa Mose potuluka mu Ejipito.

-Chifukwa chakuti Mulungu anakonza zoŵatsogolera a Isirayele kuditira mwa Mose potuluka mu ukapolo.

-Mulungu anadziŵa kuti Mose adzakhala otetezedwa bwino mnyumba ya Farawo.

-Mulungu anadziŵa kuti Mose adzaphunzira kulemba ndi kuŵerenga mnyumba ya Farawo.

-Mulungu anadziŵa kuti Mose adzaphunzira zinthu zina zambiri mnyumb ya Farawo zimene zidzamuthandize iye poŵatsogolera a Isirayele.

-Farawo ankafuna kuti aŵawononge a Isirayele, koma Mulungu anaŵatchinjiliza iwovo.

-Kodi pali munthu amene angayiletse tchito ya Mulungu?
-Palibe.

-Satana ndi ziwanda zake nazonso zinkafuna kuŵawononga a Isirayele koma Mulungu anaŵatchinjiliza iwovo.

-Kodi pali chiwanda chimene chingayiletse tchito ya Mulungu?

-Palibe.

-Chomcho, Mulungu anaŵapatsa makolo ake a Mose nzeru zomuyika mwana wawo mkadengu kakang'ono, ndipo anakakabisa mu tsinje wa Nayilo.

-Kodi Mulungu anamuteteza mwana wawo, Mose?

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:5-10

5-Tsiku lina mwana wamkazi wa Farawo anapita ku mtsinje kukasamba. Iyeyo anali ndi adzakazi ake, ndipo onsewo ankangoyenda m'bali mwa mtsinje muja.

Tsopano mwana wa Farawo uja anakawona kadengu kaja m'mabangomo, ndipo anatuma mdzakazi wake kuti aka-katenge.

6-Atakatsegula kadengu kaja, anapezamo kamwana kakamuna kakungolira. Mtsikanayo anachita nako chifundo kamwanako, ndipo anati, 'Kameneka ndi kamwana ka Chiheberi.'

7-Apo mulongo wake wa kamwanako anafunsa kuti, "Bwanji ndikakuyitanileni mayi wa Chiheberi woti akakulerereni mwanayu?" Mwana wa Farawo uja adayankha kuti,"

8-Chabwino, pita." Mulongo wake uja anapita kukawayitana mayi ake a mwanayo.

9-Tsopano mwana wa Farawo uja anamuwuza mayiyo kuti, "Mutengeni mwanayu, mukandilerere, ine ndidzakulipirani." Chomcho mayi uja anamutenga mwanayo, ndikumakamulera.

10-Mwana uja atakula anakamuperekwa kwa mwana wa Farawo uja, ndipo adasanduka mwana wake ndithu. Mwana wa Farawo anamutcha kuti Mose, chifukwa adati, "Ndidamuvuwula m'madzi."

-Mulungu anatumiza mwana wa mkazi wa Farawo oyipa uja kukamupulumutsa Mose.

-Satana amadana ndi inu nonse.

-Satana safuna kuti inu mudzimvera uthenga wa Mulungu.
-Satana amafuna kuti nonse mudzapite ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Ngakhale kuti Satana ankafuna kuŵawononga a Isirayele, Mulungu anaŵatchinjiriza iwovo.

-Ngakhale kuti Satana ankafuna kuŵawononga a Isirayele, Mulungu anaŵadalitsa iwovo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵadalitsa a Isirayele?

-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵakonda a Isirayele.

-Chifukwa chakuti Mulungu sankafuna kuti aphwanye Ionjezo Lake kwa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:12-14

12-Koma a Isirayele ankati akamaŵazunza kwambiri, ndi pamene iwo ankachulukirachulukira, mpaka adabalalikira m'dziko lonselo. Chomcho a Ejipito ankaŵawopa kwambiri a Isirayele,

13-ndipo ankaŵakakamiza mwankhaza kugwira tchito ya ukapolo.

14-Moyo wa a Isirayele unali owawa chifukwa cha tchito yakalavula gaga yowumba njerwa, ndiponso ntchito zosiyanasiyana za ku minda. Ankaŵakakamiza kugwira tchito mwa nkhana tchito zonse zolemetsa.

-Kenako, tsiku lina Satana anamupatsa Farawo maganizo ena oyipanso.

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 1:15-22

15-Tsopano mfumu ya ku Ejipito ija, idayitana azam-
ba amene ankawathandiza azimayi a Chiheberi pochira..
Wina mwa azamba ameneŵa anali Sifira, wina anali Pu-
wa. Mfumuyo inaŵawuza azambawo kuti,

16-“Mukamaŵathandiza azimayi a Chiheberi pochi-
ra, akabadwa mwana wa mamuna, mupheni, akabadwa
wamkazi mulekeni.”

17-Koma azambawo ankawopa Mulungu, koter
kuti mawu a mfumu aja sadaŵasamale konse, ana
amunawo ankangoŵaleka a moyo.

18-Tsopano mfumu ija inaŵayitana azamba aja
ndikuŵafunsa kuti, “Chifukwa chiyani mukuŵaleka ana
amuna osaŵapha?”

19-Azamba aja anayankha kuti, “Azimayi a Chi-
heberi safanana ndi azimayi a Chiejipito. Iwo ndi am-
phamu kwambiri, amati mzamba asanafike, mwana ama-
khala atabadwa kale.”

20-Chomcho Mulungu anaŵakomera mtima azam-
bawo, mwakuti a Isirayele anapitilirabe kuchulukana, na-
khala amphamu kwambiri.

21-Tsopano chifukwa chakuti azambawo ankawopa
Mulungu, Mulungu anaŵapatsa mabanja.

22-Pamenepo Farawo anaŵalamura anthu ake kuti,
“Mwana aliyense wamamuna wobadwa mwa a Heberi, az-
imuponya mu mtsinje wa Nayilo.koma ana onse akazi
adziŵaleka, azikhala ndi moyo.”

-Kodi maganizo ena oyipa amene Satana anapereka kwa
Farawo anali otani?

-Satana anapereka maganizo akuti ana onse amuna a a
Isirayele adziphedwa.

-Kodi Mulungu anadziŵa zakuti Satana wakhoza
zoŵawononga a Isirayele?

-Inde.

-Kodi Mulungu anakalora kuti Satana aŵawononge a
Isirayele?
-Iyayi.

-Mulungu anaŵayang'anira ndikuŵatchinjiliza a Isirayele.

-Mulungu anakonzanso zoŵatulutsa a Isirayele mu dziko
la Ejipito ndikubwerera nawonso ku dziko la Kanani.

-Mulungu anakonza zoŵatulutsa a Isirayele mu dziko la
Ejipito ndikubwerera nawonso ku dziko la Kanani kuitira
mwa munthu wamamuna dzina lake Mose.

-Apa pali nkhani ya Mose:

Tiyeni Tiŵerenge Ekisodo 2:1-4

1-Munthu wina wa fuko la levi, adakwatira mkazi wa
fuko lomwelo.

2-Mkaziyo adatenga pathupi, nabereka mwana
wamamuna. Atawona kuti mwanayo ndiwokongola kwam-
biri, anamubisa miyezi itatu.

3-Koma mwanayo atafika pa msinkhu wakuti san-
gathe kumubisanso, mayiyo anatenga kadengu ka bango,
nakamata phula. Tsopano mwanayo anamuyika
m'menemo, nakayika kadenguko pakati pa bango lalitalili-
tali m'madzi, pafupi ndi chibumi cha mtsinjewo.

4-Ndipo mulongo wake wa mwanayo anayimilira pa-
fupi ndikumapenyetsetsa, kuti awone zimene zingamuchi-
tikire mwanayo.

-Mayi ndi bambo ake a Mose ankakhulupilira mwa Mulun-
gu.

-Mayi ndi bambo ake a Mose ankakhulupilira kuti Mulungu
adzamuteteza mwana wawo.